TAPE NO. B4164.N.Z. 12/94

KUIKA MAZIKO 5

Chiphuzitso cha Maubatizo

Chabwino ambiri, a inu simukhala odabwa kuti tiyamba ndi kulengeza. Ndipo kupitilira apo tikufunsani kuti tinenere limodzi munthawi yotsatila. Ichi chatengedwa ku Akolinto 6:11 yomwe imayamba ndi "Ndipo otere anali ena a inu". Ndiyetu "Ndipo otere anali ena a inu" ikukamba za mndandanda wa machimo oopsa omwe anthu adatsutsika nawo. Koma timayamika Mulungu, kuti pali koma. ndima yamika Mulungu chifukwa cha ma "koma''mBaibulo. Ndipo likunena kuti;

….koma munasambitsidwa, koma munayeretsedwa, koma munayesedwa olungama mdzina la Ambuye yesu khristu, ndi mwa mzimu wa Mulungu wathu.

Chabwino, Rute ndi ine timakhulupilila Kupanga izi kukhala za iwe Mwini kotero tisiya mawu akuti 'Ndipo otere anali ena a inu'ndipo tiyamba ndi mawu akuti ''koma'' ndipo tiyipanga kukhala umboni wa iwe Mwini.

Koma tinasambitsidwa, koma tinayeletsedwa, koma tinayesedwa olungama mdzina la Ambuye yesu khristu ndi mwa mzimu wa Mulungu.

Kotero tsopano tikupatsani mwayi kuti mupange pamodzi ndi ife ichi ndi chosavuta kuchikumbukira. chimayamba ndi "koma ife.''

koma ife tinasambitsidwa,koma ife tinayeretsedwa, koma ife tinalungamitsidwa mu Dzina la Ambuye Yesu Khristu, ndi mwa Mzimu wa Mulungu .

Amen. Mulungu akudalitseni.

Tsopano tikupitilila ndi Phunziro laziphunzitso za maziko zomwe zafotokozedwa ku Ahebri 6:1-2.

Taphunzila kale maphunzilo awiri oyamba, kutembenuka mtima kuloza kwa Mulungu ndi chikhulupiriro mwa Ambuye Yesu Khristu.Ndipo tsopano tipita ku chiphunzitso cha maubatizo. Ndingowerenga mau amenewa mwachidule kuti titsimikize kuti tazikika pa mau enieni a Mulungu. Ahebri 6;1-2.

Mwa ichi polekana nawo mau achiyambidwe [ndikakonda kunena kuti maziko achoonadi] chikhristu, tipitirire kutsata ukulu msinkhu [kukhwima, omalizika] osaikanso maziko akutembenuka mtima kusiyana nazo ntchito zakufa, ndi a chikhulupililo cha Mulungu.

Ndipo chiphunzitso cha chitatu chomwe tikhale tikuphunzira m'mawa uno, chiphunzitso cha maubatizo.m'malo mwa chiphunzitso munganenenso kuti Kuphunzitsa za.Ndipo onani kuti mau akuti ubatizo akusonyeza kuti ndi ambiri.Pali oposa ubatizo umodzi. Zenizeni ndizakuti, pali maubatizo amitundu itatu omwe akufotokozedwa mu chipangano chatsopano ndipo tikhala posachedwa tikhala tikuphunzira lililonse la iwo.

Ndisoweka kunena pang'ono poyamba pa zonse-chabwino, ndiloleni ndingolankhula mwachidule za zinthu zokhuza maubatizo atatuwa. Woyamba, ubatizo wa Yohane,ubatizo wa Yohane Mbatizi.Wachiri, Ubatizo wa chikhristu omwe siuli ofanana ndi wachitatu, Ubatizo wa Mzimu Woyera ,onse amenewa amatenga gawo lofunika muchipangano chatsopano.

Tsopano ndisowekera kunena chinthu china chake chokhuza tanthauzo lamau akuti ubatizo. Siliu lachingerezi kwenikweni, ndila chi griki lolembedwa muzilembo za chingelezi. Chomwe zilembo zilankhula, monga kumasulila bwinobwino

Mau akuti limatengedwa kuchokera ku liu la chigriki lakuti, baptizo koma kuti silimangotanthauzidwa koma linalembedwa mu zilembo za chingerezi. Monga mwa zomwe zinachitika, pali zotheka kuchitika zingapo. Zikhonza kukhala kuti chinali mwambo wa chipembezo kapena zikhonza kutheka kuti omasulira baibulo la King James Version la chingelezi sadafune kukhumudwitsa mpingo wa Angrican pakubwera nditanthauzo loyenera la liu limeneli. Sindikudziwa ndipo koma sindikutsindika pa lingaliro lina lili lonse.koma, mukabwera ku chigriki palibe funso lina lili lonse pa tanthauzo lolondola la mau awa, limatanthauza kumiza. Ndipo mukhoza kumiza mu njila ziwili ndipo njilazonse ziwrizi ndizongogwirizana ndi chipangano chatsopa.mungathe kumiza pakuika chinthu pansi pa madzi kotero kuti chibisike kwanthunthu, kapena mungathe kumiza chinachake mwa kuthila madzi pa icho.koma njila inaili yonse yomwe mungachite, ndi yathunthu, si ili yoperewera.

Ubatizo kwenikweni ndi chobweretsa kusintha. Ubatitzo wa mtunduwina uliwonse omwe wakambidwa muchipangano chatsopa umaimila kusinthika. Mumachoka mu chinthu china kulowa mu china, munthu yense amasuntha, osati mbali imodzi ya inu.Chifukwa cha ichi ndikhulupilila kuti ndikofunika kutsindika kuti ubatizo ndi kumiza kwathunthu. Si mbali imodzi yokha imene imakhuzidwa, ndi chochitika cha ubatizo.

Tsopano liu likugwiltsadwa ndi ena omwe amawonjezeredwa koyambilira. Ndipo kotero tisowa kuti tifotikoze izi. Limagwiritsidwa ntchito ndimau onjezera [''mu'' ndipo amaonjezeredwa liu lakuti] ''mu'' kapena nthawi zina 'ku'. Mau oonjezera amakamba za chipagawo Chomwe inu mukubatizidwa. Angathe kukhala madzi kapena angahte kukhala Mzimu Woyera. Mawu akuti, 'mu' afotokoza zachotsatira chomariza chaku kubatizidzwa. Kodi mumadutsa muchayini monga chotsatira cha ubatizo? Mwachitsadzo, Yohane mbatizi wubatizo wake wunali wa madzi, kuloza ku kutembenuka mtima, kapena chikhululukiro cha machismo. Kotero pali 'mu' ndi 'mkati'.Wubatizo wa Mzimu Woyera, womwe sitikamba posachedwapa, uli mu Mzimu ndipo uli

wakulowa mthupi la Yesu Khristu. Tibweranso ku ichi pambuyo.Koma pomwe mukulingalira za wubatizo muyenera kufusa mafuso awiri awa: Kodi ndi muchani ndipo ndikulowa mu chain?

Tsopano tiyeni tione za ubatizo wa Yahane, ubatizo wa Yohane Mbatizi yemwe adapeza dzina lake kuchokera ku chowona chakuti anali obatiza. Izi zikukambidwa ku Marko 1:2-5.

Monga mwarembedwa mu Yesaya m'neneri, Ona nditumа mthenga wanga patsogolo yankhope yanu, Amene adzakonza njira yanu. Mawu wofuula mchipulu. Konzani khwalala la Ambuye.lungamitsani njila zake.

Uwu unali utmiki wapadera wa Yohane mbatizi. Ayenera kupita patsogolo pa Messiah ndikukonza njira yake. Uthenga makamaka unali wophweka, ukadakhonza kupatsidwa dzina limodzi. Lapani. Likunena mu ndime yotsatira.

Yohane anadza nabatiza mchipululu, nalakila ubatizo wa kutembenuka mtima wakuloza ku chikhululukiro cha machimo.

Koma mawu akuti kuloza ku chikhulukiro cha machimo.

Kotero anabatizidwa ndi ndi ubatizo wa kutembenuka mtima omwe unawatsogolera ku kulapa ndi chikhululukiro cha machimo. Kubatizidwa mu madzi kulowa mu chikhululukiro cha machimo.

Ndipo cholinga cha ichi chinali chakuti akonzere njira ya kubwera kwa Messiya wa Israel anamudikilila kwa nthawi yaitali, Yesu wa ku Nazareti. Ndiganiza kuti ndizachidziwikire kuti Yesu sakadabwera, Mulungu sakadammasula Iye kuti iye abwere, mpaka mitima ya anthu a Mulungu idali itakonzekeratsedwa mwa kulapa. Ndipo ndikuganiza kuti zomwezi ndi zoona pa kubweranso kwachiwiri kwa Yesu. Mitima ya anthu a Mulungu iyenera kuti ikukonzekeretsedwa mwakutembenuka mtima. Ndiganiza pena pake kuti kutembenuka mtima ndiwo uthenga umodzi wofunika omwe anthu a Mulungu lero akuusowa, iri ndi nganizo chabe.

Utumikiwa Yohane unalinso wofunika kuti ulumikize zochitika zanthawi ziwiri za zochititika za Mulungu, kapena zochitika ziwiri, nthawi ya chilamulo ndi aneneri ndi nyengo ya chisomo ndi uthenga wabwino, yomwe idza ndi Yesu. Kotelo Yohane ndi munthu wofunika mu kusintha konse kwa cholinga cha Mulungu. Timadziwa pang'ono za iye ndipo ine Mwini ndikuvutika ndipo ndikuganiza ndikuchepetsa kufunika kwa utumiki wake. Utumiki wake wa nthawi yochepa koma unali ofunika kwambiri. Unakonzera njira ya Yesu. Mphamvu yake pa anthu. Mukuyang'ana mundime yotsatirayo ya marko 1:5 imati:

Ndipo natuluka aku dziko lonse la Yudeya, ndi aku Yelusalemu onse, nadza kwa iye abatizidwa ndi iye mu mtsinje wa Yordano poulula machismo awo.Kotero munthawi yochepa afikila anthu mazana azikwi osakaika, anthu onse aYelusalemu, Yudeya ndi madera ena.

Ine nthawi zonse ndimalingalira za momwe Mulungu amachitira zinthu. Saitanitsa bungwe, kubwereka bwalo la mpira, kupanga gulu loimba ndi kunena, "Tikhala ndi msonkhano." Amachita izi mu njira yosayembekezereka. Kotero kuti muthu m'modzi wovala chovala cha ubweya wa ngamila anapita mchipululu, muthu m'modzi yekha. Anthu onse anatuluka kupita kwa iye. Mukuona, iyi ndiyo yomwe ikuoneka kuti ndi njira yomwe Mulungu amachitira zinthu. Amachita zinthu munjira yosayembekereka. Ndipo Chomwe chimabweretsa anthu si makonzekeredwe, ngakhale kuti timayamika Mulungu chifukwa chamakonzekeredwe, si malengezedwe, si mafalitsidwe, ndi kuyenda kodabwitsa kwa Mzimu wa Mulungu. Ndipo mukudziwa chomwe tisowa? Tisowa chomwecho lero. Pomwe moto wa Mulungu ukuyaka, anthu adzapita, ziribe kanthu kuti malo ake ndi owoneka bwanji, ziribe kanthu kaya ndi ophunzira kapena osaphunzira. Monga momwe ife tidziwira, Yohane Mbatizi adalibe maphunzilro a sukulu ya Baibulo koma anali munthu woyaka ndi moto wa Mulungu. Yesu analankhula kenaka kwa anthu a nthawi yake,''Anali nyali yoyaka ndi yowala, ndipo inu munafuna kukondwera mkuunika kwake.''Koma zomvetsa chisoni anthu ao omwe Yesu amalankhula kwa iwo sanalandire motowo. Anapita ku kuwala, analandira ubwino wa kuunikako. Koma sanalandire motowo.

Ndemanga ya Yesu ya Yohane ndi yamphamvu kwambiri. Anali nyali yoyaka ndi yowala. Ndikukhulupirira izi ndizoona mwa sayansi kuti ngati ufuna kuwala uyenera kuyaka. Palibe kuunika kopanda kutentha. Kotero tiyeni tonse titengere izi ku mtima. Ngati tingawale chifukwa cha Yesu tiyenera kuyaka, tiyeni tipemphere kuti tikhale pomwe Mulungu angaike kuunika kowala ndi koyaka.

Monga ndanena kale, ubatizo wa Yohane unali muchikhululukiro cha machimo. Anali kulumikizitsa nyengo ya chipangano cha kale (chilamulo) ndi chipangano chatsopano (chisomo). Yesu akuzitulutsa izi mu Mateyu 11:13 kulakhula za Yohane kuti:

"Pakuti aneneri onse ndi chilamulo chimanenera kufikira pa Yohane"

Yohane anali chimaliziro cha nyengo yakale. anali olumikizitsa kunyengo ya tsopano ndi wa chisomo cha uthenga. Koma izi zikumupangitsa munthu wofunika. Mwa kumveka kwina anang'amba pakati mbiri ya anthu a Mulungu. anamaliza nyengo imodzi ndikuyambitsa ina . Ndakhala kawirikawiri ndi kuganiza pa ine ndekha kotero sindinayamikile kwanthunthu za kutchuka kwa Yohane Mbatizi. chifukwa Baibulo silimalankhula kwambili za iye. Koma zonse zomwe limanena ndi zomveka bwino kwambiri.

Tsopano, ubatizo wa Yohane iye ankafuna zinthu zitatu kwa anthu omwe amabwera kuti abatizidwe. Choyamba, unali ubatizo wa kutembenuka mtima. Sizongomvaimva mmoyo, ndi chisankho. Ndikufika ku mapeto achina chake, kutembenuka kuyang'ana mbali yomwe kunali kumbuyo ndi kumapita kumeneko. Yohane ankafuna kuti omwe abwera kwa iye kuti abatizidwe akwaniritse zoyenereza ichi. Poyamba chinali chisankho, kenaka ntchito yotsatila.

Chachiwiri. Yohane amafuna kuvomereza kwa machimo kwa poyera. ichi chikukhala ngati chinachoka m'malingaliro a anthu ambili mumpingo lero. Koma ndinaphunzira mwa kuona kuti ndi zamphamvu kwambiri pomwe anthu a Mulungu atsimikizidwa mokwanira ndi mzimu woyera kuti alape machimo awo. Chakhala chifungulo chomwe chayatsa zitsitsimutso zosiyana mmbuyomu, makamaka chitsitsimutso cha ku Welsh mu 1904. Chinasindikizidwa ndikuvomereza machimo kwa anthu.

Ndipo ndiloleni ndinene chinthu china chake kwa inu, simusowekera kwenikweni kuti muvomeleze machimo anu pagulu koma muyenera kulapa machimo. Chifukwa machimo okhawo omwe Mulungu wadzipereka kukhululuka ndi omwe timavomereza. Yohane akunena ku Kalata yoyamba, Yohane wina, Yohane mtumwi. Ngati tivomereza machimo athu ali okhulupilika ndi olungama kutikhululukira machimo athu.

Koma chiganizo ichi chikuyamba ndi ''ngati''. Ngati tivomereza machimo athu. Ngati sitivomereza, tiribe chitsimikizo chakuti Mulungu atikhululukira.

Ndakhala ndikuthandiza ambili, ambili a okhulupilira muzaka zambiri omwe ali ndi machimo ambili osavomeredwa kumbuyo kwa moyo wao. Ndipo amabwera kufuna machiritso kapena dalitso ndipo amadabwa chifukwa chomwe sachilitsidwira.

Amakhala ndi katundu wa mkulu. Davide anati; ''machimo anga ali ngati katundu olemera pa ine.'' Okondedwa, pali ena a inu pano lero omwe ali ndi katundu wolemera pa iwo chifukwa mwaunjika machimo omwe simunawavomoreze. Ena a inu mukadachita bwino kuti mukhale panokha ndi Mulungu , ndi kutsegula mtima wanu kwa Mzimu Woyera ndi kunena ''Mulungu .ndionetseni chomwe ndiyenera kuvomereza.'' Koma chonde kumbukilani zomwe ndanena, ngati simuvomereza, mulibe chitsimikizo chakuti Mulungu akhululukirani. Ngati muvomereza iye akhululuka.

Chinthu chachitatu Chomwe Yohane amafuna ndicho umboni wakusinthika kwa moyo. Ankafuna kuti pakhale umboni wakuti anthu atembenuke mtima. Anthu akafika kwa iye omwe sadatembenuke mtima amakana kuwabatiza. makamaka awa anali anthu achipembedzo a nthawiyo –Afalisi ndi Asaduki. Yesu adawafotokozera Afalisi pamenepo, Anati ''Anthu wamba, amsonkho, ndi mahule anakhulupirira Yohane koma inu sinakhulupirire.'' Anati ''azakutsogolerani kulowa mu ufumu wa kumwamba ''Ndizachikhalidwe, ndi zovuta kwa anthu ozama muchipembezo kuti afike kulandila chofunika chatsopano cha Mulungu. Ndalankhula nthawi zina pomwe kuyenda kwatsopano kwa mzimu kubwera mu mpingo kumaonjezela mbili yatsopano ku chinyumbacho. Ndipo kenaka, kulankhula monga wina aliyense, amaika denga pamwamba ndi kunena "ndi ichinso zithere pomwepo " ndipo nthawi yotsatila mphepo ya Mulungu iyenda, chinthu choyamba chomwe amachita ndicho kuulutsa denga lawo.

Amayesa kukhala wokwiya ndipo amaona kovuta kuti ayende ndi chomwe Mulungu angachite potsatira pake. Kotero izi zinali ngati Afarisiwo. ichi ndi chomwe Yohane ananena. Anali munthu wolankhula mosabisa mau.

Nthawi ina ndinakoza phunziro, sindifuna kupita mu zimenezi pano za chikhalidwe cha anthu omwe adakambidwawo iwo anali odzala ndi Mzimu Woyera.

Oyamba anali Yohane Mbatizi. Anali odzala ndi Mzimu Woyera kuchokera m'mimba mwa mai wake. Kenaka Yesu, kenaka Petro ndipo kenaka Paulo ndipo kenaka Stefano. Ndinapeza chinthu chopangitsa mantha. Ambiri a iwo anamaliza miyoyo yao mwakuphedwa. Chinthu china china chomwe ndinapeza chinali chakuti anali anthu omwe amalankhula mosabisa mau, samagwiritsa ntchito mau okoma achipembedzo.

Mzimu Woyera sangavomereze china chili chonse chomwe chaphimbidwa ndi kufunditsidwa. Amafuna kulankhula mosabisa mau. Mumvetsere chomwe Yohane ananena, alaliki ambiri sakadalankhula Choncho lero. Koma pa Mateyu 3:7-9

Ndipo iye pakuona ambiri a Afarisi ndi a Asaduki akudza kuubatizo wake, anati kwa iwo obadwa anjoka inu, ndani anakulangizani kuthawa m'kwiyo ulinkudza?

Onetsani inu zipatso zakuyenera kutembenuka mtima kapena kuyankhapo za kusinta kwa moyo ndipo musamayesa kunena mwa inu nokha Atate wathu tiri naye Abraham; pakuti ndinena kwa inu kuti mwa miyala iyi Mulungu akhonza kuukitsira Abraham ana.

Ndimfundo yodabwitsa, sichoncho? Kotero osadalira pa makolo anu, osadalira komwe muchokera. Muyenera kukumana ndizoyenera za Mulungu pa inu nokha. Kotero, izi ndizo zoyenereza za ubatizo wa Yohane Mbatizi, kutembenuka mtima kuvomereza pagulu la anthu ndichitsimikizo cha kusinthika kwa moyo.

Ndifuna ndikambe za chinachake pano chifukwa chimagwira ntchito pamalo ena ake ali onse omwe ubatizo ukugwiritsidwa ntchito. Pali kunena kwakuti anawabatiza iwo kulowa mu kutembenuka mtima. Koma, sadakawabatiza pokhapokha anali atatembenuka mtima. Kotero, ubatizo sunabweretse kutembenuka mtima, unali chitsindikizo ndi umboni wakutembenuka mtima.

Mudzapeza kuti izi ndizoona kwa malo onse omwe mau akuti ubatizo ''kubatizidwa mu'' akugwiritsidwa ntchito. Sagwiritsidwa ntchito kuti ndiwo wawabweretsa iwo mu izo koma amagwiritsidwa ntchito kuti asanyoze kuti ndiko kusindikiza pa zomwe ali. Tibwera ku izi patsogolo.

Tsopano, panali malire ku ubatizo wa Yohane. Unawatengera anthu ulendo pang'ono. Poyamba pa zonse, siunabweretse kubadwanso kwatsopano. Mateyu 11:11, Yesu akunena za Yohane Mbatizi: sanauke wa kubadwa mwa akazi munthu wamkulu woposa Yohane mbatizi, koma iye amene ali ochepa mu ufumu wa kumwamba amkulira iye.''

Kotero Yohane anali obadwa mwa mkazi koma sanali obadwa kwatsopano. Sadalowe mu kubadwanso kwatsopano chifukwa izi zinali zotheka pomwe Yesu atabwera. Kotero, anali wamkulu wa iwo obadwa mwa akazi. Koma iye amene ali wang'ono mu ufumu wa Mulungu ali

wa mkulu kwa Yohane –osati chifukwa cha zomwe ife tili koma cha pomwe Mulungu watiyika. Watifikitsa mu ufumu Kudzera mu kubadwa kwatsopano.

Mukumbukira Yesu anati ‘’pokhapokha munthu atabadwa kwatsopano sangathe kulowa mu ufumu wa kumwamba.’’ Kotero Yohane anali ndi malire, malire opatsidwa ndi Mulungu.

Chachiwiri, ichi ndi chofunika, pambuyo pa pentekoste ubatizo wa Yohane sumavomeredwa kuposa apo, sunali ofunikanso. Ichi chikuvumbulutsidwa ku Machitidwe 19, ndime zochepa zoyambirira.

Ndipo panali, pamene Apolo anali ku Akolinto, Paulo anapita pamaiko apamtunda, nafika ku Efeso, napeza akuphunzira ena, ndipo anati kwa iwo, kodi munalandila Mzimu Woyera pamene munakhulupirira?

Tsopano sitikuzidwa kuti anali ophunzira achiyani. Paulo samadziwa bwino koma anafunsa funso lomwe ndikuganiza amafunsa kwina kulikonse komwe amapita, ‘’Kodi munalandira Mzimu Woyera pomwe munakhulupirira?’’ zomwe zitsimikiza kuti ndi zotheka kukhulupirira koma osalandira Mzimu Woyera.

Mkazi wanga oyamba anali otero. Anali kambuku pazokhuza kulandira Mzimu Woyera. Nthawi zonse akakumana ndi wina aliyense amanena, ‘’Kodi munalandila Mzimu Woyera?’’

Ndipo ndiganiza kuti tili achidodo lero kuti titulutse nkhaniyi ndi anthu ‘’kodi munalandira Mzimu Woyera pomwe munakhulupirira? Chabwino Paulo anapeza china chake. Analandira kwa iye’’ sitinamumva konse kuti Mzimu Woyera waperekedwa. Ndipo anati,“ Nanga munabatizidwa nchiyani? Ndipo anati! Mu ubatizo wa Yohane.

Tsopano pali njira zosiyana zakumvetsa izi, sitinamve konse kuti Mzimu Woyera waperekedwa.” Ndi chifukwa chiani Paulo anati “nanga munabatizidwa m’chiyani? Chifukwa chiyani “nanga”? zinatheka bwanji kuti amatchedwa Akhristu koma osamva za Mzimu Woyera? Chofotokozera chimodzi ndi chomwe Yesu anauza ophunzira ake ku Mateyu 28 “Batizidwani mu dzina la Atate, Mwana ndi Mzimu Woyera.’’

Kotero, akadakhala kuti anamva za Mzimu Woyera. Kotero, Paulo anazindikira kuti anali asanabatizidwe monga okhulupirira mwa Yesu, anangobatizidwa ndi ubatizo wa Yohane.

Kotero Paulo anapitirira:”Yohane anabatiza ndi ubatizo wa kutembenuka mtima, nati kwa anthu, kuti akhulupirire iye amene anadza pambuyo pake, ndiye Yesu Khristu.”

Ndiye Paulo anati, unali ubatizo wa kukonzekeretsa koma tsopano kuti Yesu wabwera, kufa ndi kuuka kwa akufa, siwokwaniranso ai. Ndiye mu ndime 5: ‘Pamene anamva ichi anbatizidwa mdzina la Ambuye Yesu.

Ichi ndiye chinthu chofunika kwambiri, muyenera kumvomereza monga Ambuye ndi Messiah kuti muyenerezedwe pa ubatizo.

Ndipo pomwe Paulo anaika manja ake pa iwo, Mzimu Woyera adza pa iwo. Analankhula ndi maririme, nanenera.

Kotero Paulo anali atathana nazo. Sanalandire china chiri chonse chapamwamba-mwamba. Amafuna zenizenizo ndipo amafuna kuti zonse zidutse, kotero anyenera kukhala okhulupirira mwa Yesu, nabatizidwa m'madzi ndipo kenaka atabatizidwa m'madzi, ngati chochitika chotsindikika, Paulo anika manja pa iwo ndipo analankhula ndi maririme nanenera.

Kotero uku ndiye kuyesa kukhazika malire ku ubatizo wa Yohane Mbatizi.

Tsopano Tiyenera kufika ku ubatizo wachikhristu, omwe ali mau omwe ndimagwiritsa ntchito – omwe atanthauza kubatizidwa monga okhulupirira mwa Yesu. Ndikadakhoza kunena kuti ichi ndi chinthu chofunikira kwambiri koposa momwe mkhristu wapakatikati lero angazindikire. Ngakhale ma Baptist, kunena moona, ali ndi chidziwitso chochepa cha kufunika kwenikweni kwa kubatizidwa m'madzi. Ndiroreni kuti ndinene kuti simunabatizidwe mwa Yesu Khristu chifukwa muli ochimwa. Siubatizo wa kutembenuka mtima. Tiyeni tione pa Mateyu 3:13-17.

Pamenepo Yesu anachokera ku Galileya nadza ku Yordano kwa Yohane, kudzabatizidwa ndi iye koma Yohane anati ankanize nanena, Ndiyenera ine kubatizidwa ndi inu, Ndipo inu mudza kwa ine kodi?

Tsopano panthawi imeneyi Yohane samadziwa kuti Yesu anali Messiah chifukwa mu bukhu la uthenga wa Yohane akuti '' ndinadziwa kuti anali Messiayo pomwe Mzimu wa Mulungu anatsika pa iye ndi kukhala pa iye.''

Kotero uwu ndi umboni wa Yesu. Ngakhale kuti samadziwa kuti anali Messiayo, anati, "inu muli olungama kuposa ine. Sindiyenera ine kukubatizani inu.''

Koma Yesu anayankha nati kwa iye, ''

"Balola tsopano, pakuti kuyenera ife kukwaniritsa chilungamo chonse motero. "ndipo kenaka anamulola iye . kenaka Yesu, atabatizidwa, anatuluka mwa msanga m`madzi ndipo, taonani, miyamba inatsengukira iye ndipo anaona Mzimu wa Ambuye akutsika monga nkhunda ndi kutera pa iye. Ndipo mu uthenga wa Yohane amati "ndipo ankhala pa iye.

"Ndipo kenako pananza mau omveka kuchokera kumwamba, kunena "uyu ndiye mwana wanga wokondedwa mwa iyeyo ndikondwera." Ndi zosatheka kutsindika mopitilira kuti zochitika za mu Chipangano Chatsopano chimalumikizika ku kubatizidwa mu madzi. Chifukwa mu chochitika ichi onse atatu mu UMulungu anatsimikiza ichi. Yesu anadutsamo, Mzimu Woyera anatsikira pa iye mpaka atabatizidwa m`madzi , ndipo kenaka Mulungu Atate analankhula kuchokera kumwamba ndipo anati, "Uyu ndiye mwana wanga wokondedwa , mwa iyeyu ndikondwera, " Mulungu ngati mungalankhule mumulemekeze, anawelamira mmbuyo kuti atsindike za kufunika kopambana m`maso mwake za kubatizidwa m`madzi. Tsopano, ndifuna ndifotokoze za chikhalidwe cha ubatizo wa chikhristu. Siubatizo

wa kutembenuka mtima chifuwa Yesu analibe machimo omwe anayenera kulapa. Sanabatizidwe ndi chifukwa anatembenuka mtima, anabatizidwa ndi Yohane koma sanabatizidwe ndi ubatizo wa Yohane. Cholinga chinali chotani? Akunena izi yekha.

"Balola tsopano, pakuti kuyenera ife kukwaniritsa chilungamo chonse motero ".

Sakulankhullira ine akulakhulira ife. Akudzisonyeza iye mwini mmodzi wa onse omwe adzatsatila iye kudzera mu ubatizo wa m`madzi. Ndipo akunena kuti ndikoyenera ndi chofunika, ndi kukhala mu nira iyi kukwaniritsa chilungamo chonse. Ndi zomwe mumachita pomwe mwabatizidwa mu dzina la Yesu Khritsu monga wotsatira wa Yesu. Simumabatizidwa ndi ubatizo wa kutembenuka mtima. Mwatembenuka mtima koma sichifukwa chomwe mukubatizidwira. Mukubatizidwa kuti mukwaniritse chilungamo chonse, kuti mumarizitse chilungamo chonse iyi ndi mfundo yofunika kwambiri motero kuti ndifuna nditsindikepo. Ngati mutatsengula ku Aroma 5: 1 Paulo akunena za ife okhulupirira mwa Yesu.

Popeza tsono tayesedwa olungama ndi chikhulupiriro, tikhala ndi mtendere ndi Mulungu mwa Ambuye wathu Yesu Khritsu.

Kotero Paulo akunena kudzera mu chikhulupiriro chathu mwa Yesu talungamitsidwa. Ichi ndi chimodzi cha chofunikira kwambiri mu Chipangano Chatsopano, koma chomwe chiri chosamvetsetseka bwino bwino. Ndinena kuti liri ndi matathauzo osiyana angapo: kusapezeka ndi mlandu, olengezedwa kuti sanalakwe, owonetsedwa olungama, opangidwa olungama. Liri ndi matathauzo onsewo, koma kudzera mu chukhulupiriro chathu mwa Yesu tinapezeka osalakwa, talengezedwa osalakwa, tayesedwa olungama, ndipo tapangidwa kukhala olungama. Ndipo ndicho chifukwa chake tiyenera kubatizidwa osati chifukwa cha kuti tatembenuka mtima kuchoka ku machimo athu koma chifukwa ndi njira yokwaniritsa chilungamo . tiri kale ndi chilungamo choyikidwa kwa ife kudzera mu chikhulupiriro chathu mwa Yesu, tsopano ubatizo wa madzi ndi njira yoyenera kukwaniritsa, kumalizitsa kapena kutengera chilungamocho.

Ndinganiza kuti ichi chomvetsetseka pang`ono kwambiri lero. polakhula mosavuta, monga ndalankhula, kwa ubatizo wa madzi ndi kodziwika pang`ono. mtundu wa yankho lomwe mungalandire ndi lakuti, "chabwino, ngati mufuna kubatizidwa tikhala ndi mwambo wa ubatizo mu masabata awiri akubwerawa, lembetseni, dzina lanu. "iyi sinjira yomwe Chipangano Chatsopano chimachitira ndi ubatizo. Ndikuonetsani ichi.

Tsopano ubatizo makamaka ndi kudzipereka. Ndikukamba za ubatizo wa chikhritsu ndi kudzifananiza ndi Yesu mu imfa yake kuikidwa m'manda ndi kuuka kwa akufa, Aroma 6:3.

Kapena kodi simudziwa kuti ife tonse amene tinabatizidwa mwa Khritsu Yesu, tinabatizidwa mu imfa yake, chifukwa chake tinayikidwa m'manda pamodzi ndi iye mwa ubatizo kulowa mu imfa , kuti monga khritsu anaukitsidwa kwa akufa mwa ulemelero wa Atate, chotero ifenso tikayende m`moyo watsopano.

Kotero ubatizo wa chikhritsu, ndicho kudzifananiza ndi Yesu mu imfa, kuikidwa m`manda ndi kuuka kwa akufa. Tinafa ndi iye mu manda a madzi tinaikidwa m`manda pamodzi ndi iye, ndipo kenaka kutuluka m`manda a madzi timauka ndi iye kuti tiyende mu moyo watsopano, moyo wa mtundu wina wosiyana ndi omwe timakhala mbuyomo. Ndipo Paulo akunena anaukitsidwa kuchoka kwa akufa ndi ulemerero wa Atate. Koma mukabwerera ku Aroma 1:4 mupeza kuti anaukitsidwa kwa akufa ndi Mzimu Woyera, kotero, pomwe tibatizidwa zimasonyeza kuti tafika ku mapeto a moyo wa ife eni.

Tafika ku mapeto kwa kuchita zithu mu kuthekera kwathu ndi chilungamo ndi mphamvu, kuchokera tsopano kupita mtsogolo tidzakhala monga Yesu. Tikatuluka m`manda, manda a madzi, ndiko kuti tiyende mu mphamvu ya Mzimu Woyera. Yesu sanadziwukitse yekha kwa akufa. Izi ndizodziwika bwino. Anawukitsidwa kwa akufa ndi Mulungu Atate kudzera mwa Mzimu Woyera. Paulo akunena ku Aroma 1:4.

Amene anatsimikizidwa ndi mphamvu kuti ndiye mwana wa Mulungu monga mwa Mzimu wa Chiyero ndi kuwuka kwa akufa, ndiye Yesu Khritsu Ambuye wathu.

Mabwalo amilandu awiri osiyana - limodzi la Chiyuda, limodzi la chiRoma – anamuweruza kuti aphedwe monga wambanda, koma pa tsiku lomaliza pomwe manda anatseguka ndipo anauka kwa akufa, Mulungu anabweza zisakho zao. Anati, “uyu ndi mwana wanga. ali mu njira zonse olungama ndipo ndikumubweretsa ku moyo chifukwa adzakhala woyamba wamoyo ndi uMulungu kwa iwo onse omwe adzakhulupirila iye, “oh, nkofunika bwanji kuukanso kwa akufa kawiri, ndipo inu onani mu madzi timachita zoona za kuukanso.

Ndinali mphunztsi wa ophunzira a ku Africa zaka zapitazo, kuwaphunzista kuti akhale aphunzitsi. Ndipo chenicheni ndinawauza ichi. “Anthu amakumbukira magawo atatu pa khumi a zomwe amamva, magawo asanu ndi limodzi pa khumi a zomwe amva ndi kuona, ndi magawo asanu ndi anai pa khumi a zomwe amamva, kuona ndi kuchita, kotero, osangowasiya ophunzira anu kungokhala pa mpando kumvetsera mu china chake, muziwapangitsa kutengapo mbali pa kuchita china chake chosonyeza kuti amva china chake, chosonyeza kuti amva zomwe mwawaphunzitsa. ndipo Mulungu amatsatira dongosolo lomwelo. Kotero sumangophunzitsa chidziwitso chabe, amatilola kuti tione zinthu ndipo amatilola kuti tichite zinthu. Ubatizo wa m`madzi ndi kuchita chinthu chochita chatsopano, nthawi zonse chimachitika kutenga malo a imfa, kuikidwa m`manda ndi kuuka kwa akufa kwa Yesu Khritsu. Ndipo mu mpingo woyambirira simukadalowa mu Tchalichi pokhapokha mutadutsa chochitika cha chikhulupiriro chomwe munavomereza onani, sikunakwanira kokha kungonena kuti, “Ndikhulupirira, “anayenera kuchita chikhulupiriro chao.

Tsopano, pomwe mwaikidwa m`manda ndikuukanso, moyo wanu sukhalanso wanu. Ngati mufuna kupitirira kukhala moyo wa inu nokha simuyenera kubatizidwa chifukwa ndi chigamulo

cha imfa yanu. ndipo kenaka ndi kuukanso kwanu. Koma pomwe mwaukitsidwa moyo wanu sukhala wanunso. Mukuona? Ndikudzipereka ku umbadwa.

Mu Mateyu 28, kumapeto a mutuwu Yesu anawuza ophunzira ake zomwe anayenera kuchita polalika uthenga wake. Mateyu 28: 19 – 20, Anati,

Chifukwa chake mukani phunzitsani anthu a mitundu yonse ndi kuwabatiza iwo mdzina la Atate, ndi la mwana, ndi la Mzimu Woyera, ndi kuwaphunzitsa asunge zinthu zonse zimene ndinakulamulirani inu masiku onse kufikira chimaliziro cha nthawi ya pansi pano.

Kotero, ananena pitani ndikupanga ophunzira a mitundu yonse. Sanatiuze ife kuti tipange mamembala a Tchalitchi, kodi munachiona ichi? Kodi mukudziwa vuto lalikulu kwambiri mu mpingo lero? Ndi mamembala a Tchalitchi omwe sali ophunzira. Chifukwa sakhala monga kufunikira mu choonadi chomwe ife tikuchilalikira. Ngati simuli ofuna kukhala ophunzira, mulibe ufulu wakuti mubatizidwe.

Ubatizo ndiwo kudzipereka ku kuphunzitsidwa. Sadataye nthawi yitali kuwaphunzitsa iwo asanabatizidwe, koma pomwe anadzipereka kenaka amawaphunzitsa iwo. Taonani, apatu zikumveka bwino, chifukwa chiyani kutaya nthawi kuphunzitsa anthu omwe asanadzipereke? Atsimikize kudzipereka kwao ndipo yambani kuwaphunzitsa zomwe ayenera kudziwa.

Taonani, ndadutsa mu izi pomwe ndinali wa mishoni ku m'mawa kwa Africa. Amatenga masabata kuphunzitsa anthu akuti abatizidwe, koma zenizeni, kumapeto kwa zomwe amachita nthawi zambiri ndiko kubatiza anthu achikunja. Amapeza chidziwitso cha m'mutu, sanakhale ndi kusinthika kwa mumtima. Sanadzipereke kwathunthu kwa Yesu. Ndinatsogozedwa kuti ndichite kafukufuku wa izi ndipo ndikuwonetsani posachedwapa.

Koma tsopano tiyeni tiringalire za zoyenereza za ubatizo wa chikhritsu. Taphunzira za zoyenereza ubatizo wa Yohane M`batizi, tiyeni tiphunzire za zoyenera za ubatizo wa chikhritsu. Yesu anati, poyamba pa zonse, pitani mupange ophunzira a dziko lonse, muwabatize awo, kotero munthu yemwe ayenera kubatizidwa ayenera kuti anamva uthenga wabwino wa Yesu Khristu. Mukumbukira za zomwe ndinanena kuti uthenga wabwino uli chiyani? Ndimfundo zitatu za mbiri Yesu anafa, anayikidwa m'manda, anawuka kwa akufa. Ngati mukhulupirira ichi, zimawerengedwa kwa inu kuti ndi chilungamo. Mumalungamitsidwa kotero, tiribe ufulu wa kubatiza anthu omwe sadakumane ndi zochitika zophweka za uthenga wabwino.

Chachiwiri, choyenereza china ndicho kutembenuka mtima. Pa Tsiku la Pentekoste mu Machitidwe 2:38 timawerenga za kuyankha kwa Petro pomwe gulu la anthu otsutsika koma osatembenuka adanena kwa iye.

"Tidzachita chiyani, amuna abale "ndipo Petro anayankha mu ndime 38 "lapani"

Mukukumbukira zomwe tinanena, kulapa [kutembenuka mtima] ndicho chochitika choyamba.

Lapani, batizidwani yense wa inu m'dzina la Yesu Khritsu, kukoza ku chikhululukiro cha machimo anu, ndipo mudzalandira mphatso ya Mzimu Woyera.

Iyi ndiye ndondomeko ya Mulungu, zonse ziri mu ndime imodzi, chifukwa chiyani tikuyigawa ndi kuyisiyanitsa ndi masabata kapena miyezi? Ndinali mbuli pokhuza za uthenga wabwino kotero kuti pomwe ndinapulumutsidwa, ndinabatizidwa mu Mzimu. Sizinachitikire mtchalichi, zinachitika mu chipinda cha nyumba ya asilikari. Ndinaphunzira pambuyo pake kuti muyenera kudikira. Pa nthawi yomweyo yomwe ndinabatizidwa mu Mzimu Woyera ndinalandira mphatso ya malirime ndi kumasulira. Mulungu ayamikike kuti sindinaikidwe pamodzi ndi Akhritsu omwe ananena kuti muyenera kudikira nthawi yaitali kuti mulandire zonsezi. Petro sanakhale zimenezo, adanena kuti ndi zinthu za mphukusi limodzi, Lapani, batizidwani m`madzi, landilani mphatso ya Mzimu Moyera. Ndipo ndingathe kukuuzani, ngati mungapereke choonadi kwa anthu mu njira imeneyi, ndikuchilandira, ndi momwe zidzachitikire. Sizimatenga nthawi yaitali. Si ndondomeko yolembedwa yaitali, ndi msawutso, mu njira ina mumachoka pa muyeso wina kufika pa muyeso wina.

Chachitatu, kuti abatizidwe anthu amayenera kuti akhulupilire. Pa Mark 16:15-16 Yesu ananena kwa ophunzira ake: "Pitani ku dziko lonse lapansi, lalikirani uthenga wabwino kwa olengedwa onse".

Ndipo chochititsa manyazi ichi kwa ife kuti patapita zaka mazana awiri sitinangwire nchitoyo. Ndi mwa njira yake.

"Pitani ku dziko lonse lapansi, lalikirani uthenga wabwino kwa olegedwa onse, Amene akhulupilira nabatizidwa adzapulumuka. Kotero simukhala oyera kuti mubatizidwe ngati simunakhulupirire, muyenera kukhala okhulupilira. Amene akhulupilira nabatizidwa adzapulumutsidwa. Ndiloleni ndikusonyezeni kuti Yesu sapereka chitsimikizo cha chipulumutso kwa iwo omwe akhulupilira ndi kusabatizidwa. Mungathe kunena, "Ndizilongosola izi ndi Ambuye"

Chabwino, izo ziri kwa inu, koma mulibe lemba lakutsimikizirani za chipulumutso pokhapokha mutabatizidwa monga okhulupilira. Ndipo kubatizidwa, ndikutathauza, munthu yense kuyambira pansi mpaka pamwamba. Kumizidwa.

Choyenereza china chimafotokozedwa pa 1 Petro 3:21, akulakhula za masiku a Nowa ndipo sitipita mu zimenezo, tingotengapo zomwe zikutathauza ichi, 1 Petro 3: 20 akuti,

"Mmene inakhala yosamvera kale, pamene kuleza mtima kwa Mulungu kunalindirira, m`masiku a Nowa, pokhala kukoweka chingalawa, m`menemo owerengeka, ndiwo amoyo asanu ndi atatu anapulumutsidwa kudzera mu madzi".

Iri ndi gawo la chiganizo lofunika kwambiri, kodi sichoncho? Petro akunena Mulungu sakadatumiza chigumula cha madzi mpaka chingalawa chitapangidwa. Kotero, analindilira

mwachipiriro mpaka chingalawa chinakonzedwa, ndipo amasula chingumula. Ndipo likulakhula kuti pa anthu onse a pa dziko lapansi lero ndi angati omwe adapulumutsidwa? Asanu ndi atatu (8). Iri ndi lingaliro la pamwamba pakati pa anthu pafupifupi miyanda iwiri asanu ndi atatu anapulumutsidwa.

Chipulumutso chenicheni si cha anthu ambiri. Mafunso ambiri lero mu mabungwe amatenga, mayakho a demokalase omwe amakonzedwa ndi chisankho cha ambiri. Mulungu zinthu zake sizimamalizika mu njira imeneyo, zimayankhidwa ndi chisakho cha Mulungu.

Kotero Petro akupitirira, kulakhula za chingalawa ndipo Nowa ndi chigumula akunena kuti; palinso pali china chisiyana ndi chomwe chitipulumutsa ife tsopano, ndicho ubatizo. Kodi mukumvetsa? Akunena kuti ubatizo umatipulumutsa ife. Ndipo kenaka akuti: kosati kutaya kwa litsiro lake la thupi… sikungosamba kuti ayere… Komatu funso la chikumbu mtima chokoma kwa Mulungu.

Kotero ichi ndi choyenereza cha chinayi, Ndi chakuti mungathe kuyakha Mulungu ndi chikumbu mtima chokoma. Mu mau ena, mumanena " Mulungu, ndikudziwa ndinali ochimwa, Ndalakwa, Ndalakwa, ndikulapa, ndikhulupirira Yesu anandifera ine. Ndikhulupirira kuti kudzera mu chikhulupiriro mwa iye ndalungamitsidwa, ndayesedwa olungama. Ndachita zonse zomwe ndikanatha, Ambuye, monga wochimwa chonde ndilandireni. "Mumayankha kwa Mulungu ndi chikumbu mtima chabwino. Simungachite koposa momwe Mulungu afunsira. Ngati mwachita zonse zomwe Mulungu wafunsa, mwayakha Mulungu ndi chikumbu mtima chokoma.

Kotero tiyeni tingowonanso zinthu zinayi zomwe ziyenereza kuti okhulupirira abatizidwe. Choyamba, muyenera kuti munamva uthenga wabwino. Chabwino, muyenera kuti munatembenuka mtima (munalapa)

Chachiwiri, muyenera kuti munatembenuka mtima.

Chachitatu, muyenera kukhulupirira uthenga wabwino.

Chachinai, muyenera kukhala ndi chikumbu mtima chikoma ndi Mulungu.

Tsopano, sindikufuna mu njira ina iri yonse kuti ndikhale wa mikangano koma ndinganiza popanda mikangano iri yonse ndingathe kunena chinthu chimodzi. Mwana wakhanda sangathe kukwaniritsa zoyenereza zinayi zimenezi. Kodi ndi zoona? Ndiganiza palibe amene angakane ichi, ndi mfundo yomphweka.

Tsopano ndikubwera ku china chomwe ndinachifanizira m'mbuyomu. Kuphunzitsa chifukwa cha ubatizo sikusowekera kutenga nthawi yaitali. Taonani, ndinadutsa mu izi pa umishonale omwe ndinali. Amatenga masabata asanu ndi imodzi kuti aphunzitse otembenuka mtima ndipo kenaka ndikuwabatiza iwo. Zomwe iwo amachita ndi kubatiza achikunja ophunzitsidwa. Anthu anali akuti sanakumane ndi Ambuye, miyoyo inali yosasinthika, anali anthu a bwino koma …...

kotero ndiloleni ndingosonyeza mfundo zina zokhuza kutalika kwa nthawi. Pa tsiku la Pentekoste zikwi zitatu (3000) za anthu anabatizidwa tsiku lomwero limene linamva uthenga. Atumwi sananene, "Tsopano dikirani ndipo ngati mungabereke zipatso mu masabata asanu ndi imodzi (6) tidzakubatizani "kapena," Mukadzaphunzira ma ulaliki onse aYesu pa mtima. Anawabatiza iwo chifukwa anakwaniritsa zowayenereza, Anakhulupirira ndipo analapa ndipo anali ofuna kuti adzipereke. Onani kuti kunali kudzipereka kwa mtundu wina chifukwa anali ochepa ndithu.

Ndipo kenaka ku Machitidwe 8 mdindo wa ku Ethiopia anamva uthenga kuchokera kwa Filipo chabwino, tiyeni tiwerenge nkhaniyi ndikopindula kuyiwerenga. Chidachitika nchiyani? Machitidwe 8, mukukumbukira Filipo anali pa njira yopita ku Gaza. Anali atasiya chitsitsimutso chokodweretsa mu Samaria ndipo chifukwa mngelo anamtuma iye anali pa njira ya Gaza. Analibe ganizo liri lonse la chifukwa chimene iye anali kumeneko.

Ndipo kenaka anawona mdindo wa ku Ethiopia mu galeta wake ndipo mdindo amachita, monga ndinanene anthu amachita, amawerenga mokweza. Amawerenga kuchokera pa mneneri Yesaya. Ndipo kotero Filipo anapita kwa iye ndi kunena …. Kapena mdindo ananena kwa Filipo.

"Ndikufunsa iwe, kodi ndi za ndani zomwe mneneri anena izi? Za iye mwini kapena za munthu wina?

Amawerenga ndime ya Yesaya 53, "Anatsongozedwa ngati nkhosa kukaphedwa." ndipo mdindo anafunsa funso la nzeru, kodi mneneri akulakhula za iye mwini kapena za munthu wina? Ndipo likunena pa ndime 35:

Ndipo Filipo anatsengula pakamwa pake nayamba pa lembo iri, nalalikira kwa iye Yesu.

Mu mau ena, ananena kuti ndi Yesu yemwe Yesaya ananena za iye. Ndipo likunena iye analalikira Yesu. Filipo anali mlaliki ndipo ali chitsanzo. Uthenga wake unali waufupi. Unali wa mau amodzi. Ku Samaria analalikira Khritsu ndipo pa njira ya ku Gaza analalikira Yesu. Ndimakonda ulaliki wa alaliki oona. Ine sindine mlaliki koma nthawi zonse ndikaona mlaliki akuchitachita, china chake mwa ine chimatakasika. Ntchito ya mlaliki ndiyo kusonyeza wochimwa kwa mpulumutsi. Akachita zimenezo, ntchito yake yatha. Filipo anachita izo ku Samaria ndi kumapitirira. Anthu ambiri akadakhoza kukhalabe chifukwa unali msokhano opambana kwambiri. Koma anali ndi malangizo ochokera kwa Mulungu. Pitirira, usakhazikike. Awa anali mayeso akumvera, kotero akupitilira njira ya ku Gaza ndi mdindo uyu ndi galeta ndipo akulalikira Yesu kwa iye. Ndikufuna kuti muone kuti, analalikira Yesu.

Ndipo pamene anapitilira kuyenda anafika pomwe pali madzi, Mdindo anati, "Taonapo, madzi, chindiletsa nchiyani kuti ndisabatizidwe? "ndipo anawuza kuti aimitse galeta ndipo anatsikira onse awiri kumadzi, Filipo ndi mdindoyo, ndipo anambatiza iye.

Tsopano zikungotiwuza ife kuti Filipo analalikira Yesu koma mu kulalikira Yesu angathe kukhala kuti ananena chinthu china chokhudza ubatizo chifukwa mdindoyo anayambitsa, osati Filipo. Anati, "Taonapo madzi, chindiletsa nchiyani kuti ndisabatizidwe tsopano? Filipo anati, "Chabwino, ndichita ichi, "Ndipo onse awiri anatsikira m`madzi. Nthawi zonse pomwe ubatizo wafotokozedwa mu Chipangano Chatsopano, anthu amapita kulowa m`madzi ndipo amatuluka m`madzi.

Ndipo kenako Filipo anakumana ndi chosangalatsa anatengedwa ndi Mzimu Woyera ndipo mdindoyo sanamuonenso. Koma mdindoyo sanadandaule, anangoyenda ulendo wake alikukondwera. Koma ndiloleni ndisonyeze kwa inu kuti ndi zotheka kuti panapita ora limodzi kapena awiri kuchokera pa nthawi yomwe mdindo anayamba wamva uthenga kufikira pomwe anabatizidwa. Siyinali nthawi yayitali yakukonzekera.

Ndipo kenaka mu nyumba ya Korneliyo, mukudziwa khani yake. Petro anapita monyinyirika ku nyumba ya wa mitundu chifukwa zinali zotsutsana ndi zomwe iye amawona zokhudzana ndi chipembedzo. Koma anyamba kuyankhula kwa iwo za Yesu ndipo chinthu chodabwitsa chidachitika. Uthenga wake unadulidwa. Ndikunena kuti, "Mulungu, anatipatsa ma uthenga ena oposa odulidwa," Mzimu Woyera analowerera uthengawo. Ndipo anthu akadali kumvetsera uthengawo ikutero mdime 44:

Petro ali chilakhulire, Mzimu Woyera anagwa kwa onse akumva mawuwo. Ndipo anadabwa okhulupilirawo akumdulidwa Ayuda onse amene anadza ndi Petro, chifukwa pa amitunduwo panathiridwa mphatso ya Mzimu Woyera.

Onani, uku kunali kumizidwa. Ndibwera kuzimenezi mu phunziro lotsatira, koma uku ndi kumizidwa kwa Niagara falls (mathithi) ndi chifukwa chiyani anadabwa?

" Pakuti anawamva iwo akulakhula ndi maririme, ndi kumkuza Mulungu"

Tsopano alaliki ambiri lero amati, "chabwino tikhalabe kwa masabata asanu ndi imodzi ndipo ngati mungaonetse chipatso tidziwa kuti ndi zoona, "Tsopano, palibe m'modzi yemwe akadakhala osakonzeka kokwanira kuti akhulupirire kuti Amitundu akadakhonza kukhala okhulupilira kuposa Petro ndi abwenzi ake. Nthawi yomwe anawamva kulakhula ndi maririme anati, 'Ndi zimenezo, alandira chofanana ndi ife.'

Kenako Petro anayakha, "Kodi pali munthu akhoza kuletsa madzi kuti asabatizidwe awa, amene alandira Mzimu Woyera ngatinso ife?

Ndipo limanena kuti analamulira iwo kuti abatizidwe. Sanangoyamikira, anaulamulira. Ndichochita cha kumvera kwa Mulungu, kwa nthawi yaitali bwanji? Chabwino mwina kwa ora

limodzi kuchokela pa nthawi yomwe analakhula malirime koyamba kufikira nthawi yomwe anabatizidwa m`madzi, panalibe kuchedwetsa.

Ndipo kenaka woyang`anira wa ndende ku Filipi, Ichi ndi chinthu chapatali kwa ine. Mukukumbukira nkhani ya Paulo ndi Sila kuti anaponyedwa m'ndende yokhala ndi chitetezo champhamvu zedi, pakati pa usiku, ora la mdima kwambiri, kodi amachita chiyani? Anayimba ndi kutamanda Ambuye. Limanena kuti andende amawamva iwo, sanakhalepo ndi anthu otero kale. Ndipo pa nthawi iyi matamando awo anamasula mphamvu ya Mulungu ndipo ndende yonse inagwedera kufikira maziko, khomo liri lonse linatseguka ndipo ma unyolo a wina aliyense anagwa. Woyang`anira ndende anati adziphe yekha chifukwa pa ulamuliro wa Roma ngati mkaidi wathawa, anayenere kuyakha ndi moyo wake za mkaidiyo. Paulo anati, 'Usadzipweteke wekha' tonse tirimuno suyenera kuzipha "Ndipo likunena pa ndime 29.

"Ndipo mdindo anitanitsa nyali, natumphira mkati, alikunthuthumira ndi mantha, nagwa pamaso pa Paulo ndi Sila." Ichi ndi chodabwitsa kwambiri, sichoncho, pomwe woyang`anira ndende agwada pamaso pa akaidi?

Anawatulutsira iwo kunja, nati, Ambuye ndichite chiyani kuti ndipulumuke? Ndipo iwo anati, Ukhulupirire Ambuye Yesu, ndipo udzapulumuka, iwe ndi apabanja ako. Likunena kuti:

Ndipo anamuwuza iye mau a Ambuye, pamodzi ndi onse apabanja pake.... onse anali a msinkhu wakuti akadakhoza kumva mau Ambuye.

Ndipo anawatenga ora lomwero la usiku, natsuka mikwingwirima yao, nabatizibwa pomwepo, iye ndi a pabanja pake.

Sanayembekezere kuti kuche, zinali za changu. Sindikudziwa ngati ndinaglakhule kwa inu za kufunika kwa changu cha ubatizo wa m`madzi kunaliri kwa Akhritsu a Chipangano Chatsopano. Samadikirira, Samayembekezera kuti pakhale, mwambo wa ubatizo, chifukwa chipulumutso chawo chimangonera pa iwo. Iye amene akhulupiria nabatizidwa adzapulumuka.

Sichifukwa cha kuchita mikangano. Mungathe kusankha za momwe mungachitire kutsatira izi pa inu nokha.

Tsopano, kenaka tiyeni tione za chofunikira cha uzimu chokhudza ubatizo, mwachidule, chinakambidwa kale ku Aroma 6, tingotsegulakonso kwa kanthawi, Aroma 6 kuyambira ndime 3:

Kapena kodi simudziwa kuti ife tonse amene tinabatizidwa mwa Khritsu Yesu, tinabatizidwa mu imfa yake?

Nthawi zonse Paulo akunena "kodi simudziwa ndinapeza kuti ambiri a khristu a masiku ano sadziwa kuti ndi zochititsa chidwi. Nthawi zonse pomwe watenga chomwe alankhula kuti 'kodi simudziwa' ndinapeza kuti ambiri a Akhritsu lero sadziwa.

Anati:

Chifukwa chake tinayikidwa m`manda pamodzi ndi iye mwa ubatizo kulowa mu imfa, kuti monga Khirtsu anawukitsidwa kwa akufa mwa ulemelero wa Atate.

Chotero ifenso tikayenda m`moyo watsopano.

Kotero monga ndanena kale, timafanizidwa ndi Yesu mu imfa, ndi kuikidwa m`manda ndi zikomo Mulungu, sizithera pomwepo. Ngati tayikidwa m`manda ndi iye tinaikidwanso.

Ndipo kenako Paulo akulankhula chinthu china chofunika kwambiri. Akunena mu mdime 5; pakuti ngati ife tinakhala olumikizidwa ndi iye mchifanizidwe cha kuuka kwake.

Akulakhula za kuikidwa m`manda mu ubatizo, Akunena kuti ngati tinayikidwa m'manda potero tingathe kukhala ndi chitsimikizo kuti tidzauka, kenaka akunena:

Podziwa ichi, kuti umunthu wathu wakale unapachikidwa pamodzi ndi iye, kuti thupilo la uchimo likaonongedwe, kuti ife tisakhalenso akapolo a uchimo.

Kotero, mfundo yomwe ubatizo umasonyeza ndi yakuti pomwe Yesu anafa pa mtanda moyo wathu wauchimo, wa umunthu, wachikhalidwe cha kuwukira zinaphedwa mwa iye. Iri ndi vumbulutso. Mukuona, mungathe kukhala wowukira, ndi zomwe anthu ambiri achita, amapita ku mpingo kuvomereza machimo ao, amakhululukidwa ndipo amachoka ndi kuyambiranso kuchimwa. Ichi sicholinga cha Mulungu chifukwa chimodzi chomwe ziri choncho ndi chakuti sadziwa mfundo za mbiri zakuti Yesu anafa pa mtanda, munthu wanthu wakale, wowukira mwa wina aliyense wa kuwukira. Njira yokhayo yothetsera ndiyo kunyonga. Kunachitika koposa zaka mazana awiri zapitazo pomwe Yesu adafa pa mtanda, kotero Paulo akunena kuti muyenera kudziwa izi:

Ndipo akupitilira pa ndime 11.

Chotero inunso mudziwerengere inu nokha ofafa ku uchimo koma amoyo kwa Mulungu mwa Khritsu Yesu.

Paulo akunena kuti mudziwa ichi, ndipo muyenera kudziwerengera nokha akufa ku tchimo koma amoyo kwa a Mulungu. Ndipo zochitika za kunja ndi ubatizo wa m`madzi. Mumalowa mmanda, kutuluka m'mandamo, mumasiya moyo wanu wakale kumbuyo m`mandamo, mumakhala wolengedwa watsopano.

Chabwino tsopano, palinso ndime ina ku Akolose 2 yomwe ndiyofunika mokhudzana ndi ichi. Akolose mutu wachiwiri Paulo akulemba kwa Akhritsu, akuti mutu 2 ndime 11:

Amenenso munadulidwa mwa iye ndi mdulidwe wosachitika ndi manja, m`mavulidwe a thupi mu mdulidwe wa Khritsu.

Pansi pa lamulo la Chiyuda, mdulidwe, kunali kungochotsa gawo la thupi, koma mdulidwe wa chikhritsu ndiko kuchotsa moyo wonse wa uchimo, thupi lonse. ndipo pomwe thupi lafa, chinthu chotsatira kuchita ndi chiani? Sindikukumvani. Liyikeni m`manda, zoona ndi kulakwa kwakukulu kusiya thupi kungogona osaliyika m`manda.

Ndinali ndi a nkhondo a ku Mangalande ku mpoto kwa Africa ndipo sitinasiye mtembo pansi, nthawi zonse timawuyika m`manda. Ndipo ichi, ndiganiza ndi chithu china. Ngati mwafa, osangokhala osayikidwa m`manda. Ikidwani m`manda. Mwamvetsetsa mfundo imeneyi.

Tsopano Paulo akupitilira ku Akolose 2, mutavula thupilo, chitsatira chomwe muyenera kuchita ndi chiyani? Akunena kuti muike m`manda…… popeza mukayikidwa m`manda pamodzi ndi iye mu ubatizo, momwemonso munawukitsidwa pamodzi ndi iye m'chikhulupiliro cha machitidwe a Mulungu amene anamuwukitsa iye kwa akufa.

Onani ichi, ubatizo umagwira ntchito kwa okhulupirira okha. Ndikudzera mu chikhulupiliro chathu pa chimene Mulungu adzachita ndi momwe ife tiwukitsidwira. Ngati simukhulupilira, sizimagwira ntchito.

Tsopano ndiloleni ndikupatseni mfundo zina zofunika, Agalatiya 3: 27,

Pakuti nonse amene munabatizidwa kwa Khritsu munavala Khritsu.

Kodi timabatizidwa kulowa mchiyani? Khritsu. Sitimabatizidwa kulowa mu mpingo, kapena chipembedzo. Ichi cholakwika chachikulu. Kenanso ndibwerera ku masiku anga a ku m'mawa kwa Africa, mpingo waukulu wolakira kumeneko sukadavomera wina aliyense kuti akhale membala yemwe sadabatizidwe kulowa mu mpingomo. Munthu amatha kukhala kuti anabatizidwa moyenera ndithu monga okhulupirira, koma ngati si unali mu mpingo anayenera kuti abatizidwenso kulowa mmenemo. ichi ndi cholakwika, ndi zakuthupi. Sitimabatizidwa kulowa mu mpingo, tiyamike Mulungu, timabatizidwa kulowa mwa Khritsu.

Kenaka monga ndanena, umagwira ncthito kudzera mwa chikhulupiliro chokha. Ndipo tiyenera kuzindikira kuti moyo wathu watsopano umapatsidwa mphamvu ndi Mzimu Woyera. Mzimu Woyera yemweyo adawukitsa Yesu kuchoka kwa akufa amagwira ntchito mwa ife.

Tsopano tiyeni mwachangu titenge zithunzi ziwiri za ubatizo za Chipangano Chatsopano choyamba tachiona kale 1 Petro 3:20-21 chingalawa cha Nowa. Petro akunena chosiyana ndi ichi cha ubatizo wa madzi.

Kodi uthenga wa chingalawa cha Nowa ndi otani? Poyamba pa zonse, chiweruzo chimabwera. Panali njira imodzi yokha yopulumukira ku chiweruzo ndipo chinali chombo cha Nowa. Kotero, chingumula chiyimira chiweruzo cha Mulungu, chombo, monga mwa nthawi zonse m`Baibulo, ndi chithunzi cha Yesu Khritsu. Mu chombo mungathe kudutsa bwino lomwe amoyo otetezedwa kupitirira madzi a chiweruzo. Kunja kwa chombo mumizidwa. Palibenso njira ina yopulumukira koma kuti mukhale mu chombo, Yesu

Khritsu, ndipo mu chombo mumadutsa mu madzi muchitetezo ndipo mumaturuka kulowa mu moyo watsopano, wosiyananiratu. Moyo wa kale wakokololedwa, moyo watsopano watseguka kwa inu. Ichi ndicho chithunzi cha chombo cha Nowa.

Ndipo pali chinthunzi chinanso, chomwe tingochiang`ana mwachidule ku 1 Akorinto 10:1-2

Pakuti sindifuna kuti mukhale osadziwa, abale, kuti makolo anthu onse anali pansi pa mtambo, nawoloka nyanja onse, nabatizidwa onse kwa Mose, mu mtambo, ndi m'nyanja.

Kotero Paulo akunena mu Israeli mu Eksodo, mawomboledwe kuchoka ku Egypt, anadutsa zinthu ziwiri zowachitikira. Mtambo unatsika pa iwo kuchokera m`mwamba ndipo Paulo akuti anabatizidwa mu Nyanja. Kotero pali ubatizo uwiri omwe anakhazikitsidwira okhulupirira aliyense. Mtambo umatsika kuchokera kumwamba kufika pa inu, mumamizidwa mu mtambo, mumatsika kulowa mu madzi, kudutsa mu madzi, kudzuka kutuluka m`madzi. Ndipo pomwe anatuluka kuchoka mmadzi anayamba moyo watsopano ndi malamulo atsopano ndi mtsogoleri watsopano. China chiri chonse chinasiyidwa mbuyo.

Ndipo, anali madzi omwe anadula Aigupto. Ichi ndi chofunika kwambiri. Anapulumutsidwa ku Egypt mwa chikhulupiliro mu mwazi wa mwana wa nkhosa koma ichi sichinawalekanitse iwo kwa Aigupto. Anali madzi omwe anawalekanitsa iwo. Ndipo ndi ubatizo omwe umatilekanitsa ife. Tingathe kukhulupirira mu mwazi wa Yesu ndi kupulumutsidwa koma sitimalekanitsidwa mpaka titabatizidwa.

Ndaphunzitsapo anthu zikwi omwe adamasulidwa ku mphamvu ya mizimu yoipa. Pali ponse pomwe kunali kotheka ndimawauza iwo kuti ngati mufuna kusunga mamasulidwe anu mubatizidwe m'madzi. Chifukwa, uku ndiye kudulako. Simwazi ayi. Mwazi umakupulumutsani ku Egypt, madzi amakulekanitsani inu kwa Egypt, olekanitsidwa mwa madzi ndi mwa mtambo. Likunena kuti anabatizidwa mwa Mose, mukunena kwina, izi zinawabweratsa iwo pansi pa utsogoleri wa Mose. Chabwino ife sitinabatizidwe mwa Mose, tinabatizidwa mwa Khritsu. Khritsu anakhala mtsogoleri wathu, koma kuti tilowe mwa iye ndi mu njira ya malemba, tiyenera kudutsa pansi pa mtambo, tiyenera kudutsa mu madzi. Ndi zomveka bwino, zozindikirika bwino.

Ndipo kenaka likunena pa Ahebri 11:29, chabwino, tiwerenge apa, tiri ndi nthawi, ndinganiza choncho. Ahebri 11:29, chifukwa likutsindika za ichi kuti ndi mwa chikhulupiro chokha. Ngati muli osakhulupirira mumatsikira m`madzi wochimwa wowuma ndi kuturuka m'madzi wochimwa wonyowa. Uku ndiko kusintha kokhako kungachitike.

Ndinamva munthu akuchitira umboni kamodzi, kenaka anapulumusidwa. Anali woyimba yekha, amaimba m'tchalichi, ndipo kuti ayambe mu mpingo iwo amanena kuti "Timasowa kuti oyimba anthu kuti abatizidwe "Anati, chabwino" anali wochimwa wouma. Analowa

m`madzi ndipo anatulukamo wochimwa wonyowa. Izi ndi zonse zomwe zinachitika chifukwa panalibe chikhulupiriro. Apa likulankhula za a Israeli pa Ahebri 11:29.

Ndi chikhulupiriro anawoloka nyanja yofiyira kupita ngati pamtunda.

Anachita izi bwanji? Mwa chikhulupiriro, zoona.

….Ndipo Aigipto poyesanso anamizidwa. Chifukwa chiyani? Chifukwa analibe chikhulupiro. Kotero, ngati mubatizidwa m`madzi koma sindinu okhulupirira, zonse zomwe zimachitika ndizo mumazizidwa. Mungathe kudutsa pokhapo ku umoyo watsopano mwa chikhulupiriro mwa Yesu.

Chabwino, iri ndi phunziro lofunika kwambiri. Lofunika kwambiri koposa momwe mipingo ndi zipembedzo zidziwira lero. Ndaphunzitsa nthawi zambiri anthu omwe adatsutsika. Amati, "kodi chotsatira chomwe tingachite n'chiyani? Ndimanena, "Batizidwani, "Liti?" Mwamsanga msanga, tsopano. "Ndawatengerapo anthu ku nyanja ku Florida. Anayenera kuti ayende pa galimoto kupita ku Miami ulendo wa mitunda 20 (miles).

Ndinati, "Ndikubatizani inu koma ndiribe zovala zina. "chabwino tipita kwathu onyowa." Koma anali ataona kufunikira kwa ubatizo, kufunika kwakukulu.

Ndimafuna ndipereke ganizo iri kwa inu lakuti tiyenera kulandira kuphunzitsidwanso mu mpingo zokhudza kulingalira kwathu kukhonza ubatizo. Uli mbali ya chipulumutso. sindikukuuzani kuti ngati musanabatizidwe koma ndinu okhulupirira simudzapulumutsidwa. Izi ziri pakati pa inu ndi Ambuye. Koma ndiribe ulumuliro wakukuzani kuti mudzapulumutsidwa.

Limanena kuti, iye amene akhulupilira nabatizidwa adzapulumuka.

Ndipemphere kwa nthawi yochepa

Ambuye Yesu Khritsu, ndinu mutu pamwamba pa zinthu zonse, ku mpingo womwe ndi thupi lanu.

Tipereka kwa inu gulu la anthu awa tsopano.

Inu nokha mudziwa mitima ya wina aliyense. Inu nokha mudziwa bwino lomwe mu chiyanjano chomwe ali nacho ndi inu. Koma Ambuye, ndipemphera mowona mtima, ngati alipo omwe afunitsitsadi kuti apulumutsidwe ndi kuti akhale ophunzira, koma sanabatizidwe m`madzi, kuti muyike kufulumizidwa m`mitima mwawo mwa Mzimu Woyera kuti iwo atenge sitepe yoyenera ya kumvera. Ambuye Yesu, ichi chikhale ku ulemelero wanu ndi chifukwa cha kumanga kwa thupi lanu mu dzina lanu tipemphera, Amen